# Kukhala Moyo mwa Yesu



# ZAMKATIMU


| | | |
|---|---|---|
| **PHUNZIRO 1** | Ndine Mkhristu nanga chotsalira ndi chiyani? | **6** |
| | *(Kukula mbanja la Mulungu)* | |
| **PHUNZIRO 2** | Kukhala moyo mwa Yesu | **12** |
| | *(Moyo mwa Yesu tsiku ndi tsiku)* | |
| **PHUNZIRO 3** | Kuwerenga za Yesu | **16** |
| | *(Kuwerenga ndi kusanthula Baibulo)* | |
| **PHUZIRO 4** | Kuyankhula ndi Mulungu | **20** |
| | *(Moyo wa pemphero)* | |
| **PHUZIRO 5** | Malo opembedzera | **24** |
| | *(Moyo wa pa Mpingo)* | |
| **PHUZIRO 6** | Kuuza ena za Yesu | **29** |
| | *(Kuchitila umboni, kulalikila)* | |

## TAKULANDILANI MBANJA LA MULUNGU



Sichosangalatsa kodi kuti tsopano muli mbanja la Mulungu? Tsopano ndinu mmodzi wa mbanja la Mulungu, ndipo mudzapitilira kukhalabe ngati mumvera Yesu, kukhulupirila iye ngati Mpulumutsi wanu. Ndiso kukhala ndi nthawi yomudziwa bwino.

Mbanja la Mulungu muli atsikana,anyamata,achisodzela, ndi akulu omwe ndipo tonse ndife pa chibale Mulungu ndiye Tate wathu.

Kumufusa Mulungu kuti akhululukire machimo ako zimatanthauza kuti wakhululukidwa komaso zaiwalidwa. Chikhululukiro chimatheka chifukwa cha Imfa ya Yesu pa mtanda yomwe inapulumutsa iwe.

Ngati m'modzi wa mbanja lake Mulungu amafuna tizikhala m'moyo omukondweletsa. Tikhale moyowo ku sukulu, kunyumba, kumpingo, kosewela ndi kulikose koma mothandizidwa ndi iye.

Buku ili liku thandiza kudziwa chomwe Mululngu akufuna kwa iwe. Pokhala mbanja la Mulungu tsopano utha kuphuzila njila zomukondweletsela ndikumu tumikila Yesu Khristu ngati Mpulumutsi  wanu ndiso ngati mzanu. Ndi bukuli mudzakula mchikristu chanu mwa mphavu.

## Lowezani vesi iyi:

Luka 2:52

"Ndipo Yesu anakulakulabe mzeru ndi mu msinkhu ndi mchisomo chapa Mulungu ndi cha pa wanthu."

Udzijambule wekha mu bokosi ili

Ine ________________________________ndikuvomeleza Ambu Yesu

(dzina lako)

kukhala Mbuye ndi Mpulumutsi wanga.


Lelo pa _____________mwezi wa ________________ chaka cha

_______________________________.

Dzina la munthu yemwe wandi pemphelera:

_________________________________

Usanayambe kalikose upeze kaye Baibulo, pensulo, labala ofufutila, dikishonare [mtanthauzira mawu].





***Kagwiritsidwe ntchito kabukuli…***

1. Bukuli ugwilitse ntchito pamodzi ndi Baibulo.
2. Pemphera kwa Mulungu kuti aku thandize kuchita bwino.
3. Ukhale ndi nthawi yo welenga phunziro lililonse usanayambe kulemba pofunika kulemba.
4. Welenga funso lililose ndi ku peleka yankho lache.
5. Loweza vesi iliyose yomwe ili pa phunziro lililose.
6. Mukamaliza kuwelenga bukuli ndi kulembamo pelekani kwa aphunzitsi anu ndipo adzakubwezelani.



7. Sungani buku lanu kuti mudzawelengeso mtsogolo.
8. Onetsani anzanu bukuli mukamaliza.
9. Pitilizani kuwelenga Baibulo lanu, kupemphera ndi ku khalabe mwa Yesu.



**PHUZIRO 1**

## NDINE MKHRISTU – CHOTSALIRA NDI CHIYANI?

Anthu ena amakaikila ngati ali Akhristu, koma iwe usa kaike ngati una pempherako pemphero lomupempha Mulungu kukukhululukila machimo ako akale, ndi kumupempha Yesu kulowa mu mtima mwako.

Unakhalatu obadwa mwa tsopano, kapena kuti wa mbanja la Mulungu. Mulungu analonjeza kale izi ndipo sanganame.

Welengani malonjezo ake pa (Yohane 1:12)

Tsopano poti ndiwe wa mbanja la Mulungu uyenela kukula muuzimu ndi kukhala mkhristu wa mphamvu. Izi zinga theke pokhapokha ngati ukuwelenga ndikuphuzira mawu a Mulungu ndikuchita zowe mawu ake akufuna uchite monga mwana wake.

Mulungu samakondwela ndi zochita zathu nthawi zonse, komabe amatikondabe ndipo adzatithandiza kuti tichite zimene zili zoenela ndi zomwe iye amakondwera nazo.

"Tchimo" ndi liwu lina lotanthauza kusamvera. Tikachimwa mulungu amatisungabe mbanja lake chifukwa ndiwokonzeka kutikhululukira tikapempha kuti atikhululukire.

Mulungu amatiuza mu Baibulo zoenela kuchita ngai tikufuna kumukondweletsa.

Chimwemwe chimapezeka tikamakondweletsa Tate wathu wa kumwamba.

Pezani mavesi awa mbaibulo lanu ndipo muone zomwe Mulungu akufuna muphunzire, ndikuchita ngati mwana wake.

1. Kondani aliyese ngakhale adani anu (Mateo 5:44)
2. Khalani okoma mtima kwa aliyese (Aefeso 4:32)
3. Phuzilani kukhululukira anzanu (Luka 6:37)
4. Thandizani ena (Yesaya 41:6)
5. Usabe (Ekisodo 20:15)
6. Khalani ndi chikumbu mtima cha bwino (Ahebri1 3:18)
7. Usanene za bodza (Miyambo 12:17)
8. Velani makolo anu (Aefeso 1:6)
9. Samalitsani zoyankhula ndi zochita zanu (Luka 6:31)

Mukadzafika kumwamba simudzasowanso kuyesetsa kukhala wabwino.

Kumwambatu kulibe maesero ndi uchimo ulionse, chilichonse ndi kalikose kakumwamba ndikoyera. Mudzakhala kumwamba ndi onse ambanja lake kwa muyaya.

**Mwaphunzilapo chiyani powerenga?**

**1) Ukutsimikizika bwanji kuti ndiwe mkhristu?**

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

**2) Kopelani apa vesi yapa 1Yonane 1:9**

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

**3) Khwatchani mau osafunikila pa ziganizo zili m'musimu:**

*Usamamvere/udzimvera makolo ako.*
*Udzigawana/usamagawane ndi anzako.*
*Udzikomera mtima ena/onse.*
*Kondani/danani ndi adani anu.*

**4) zungulizani liwu loyenera:**

Mulungu anatipatsa baibulo kuti tilitsatire.

Inde/ Ayi.

Kodi mulungu amatipempha kuti tidzimvera Baibulo? Inde/Ayi

Kodi Mulungu amakondwera ndizochita zathu nthawi zones?

Inde/ Ayi.

Kodi Mulungu amatikhululukila zolakwa zathu nthawi zones?

Inde/Ayi.

Kodi Mulungu amafuna kutithandiza kuti tidzimumvera?

Inde/Ayi.

**5) Lembani dzina lanu mmizele ili mmusiyi**

Mulungu anakonda ____________________________kotero

kuti anapereka mwana wake kuti ngati

______________________ akakhulupilire iye.

______________________ akakhale nawo moyo osatha.

(Yohane 3:16)

**6) Lembani mzele kunsi kwa mawu olondola**

Liwu lina la tchimo ndi

kumvera/kusamvera/kulakwa/zoipa

**7) Ndizotheka ndizotheka kukhala moyo wa chikhritu kulikose**

Eya ayi mwina nthawi zina

**8) Yesu ndi ndani?**

Pezani yankho pa 1Yohane5:5

__________________________________________________________

**9) Yesu Khristu anafa chifukwa chiani pa mtanda?**

Werengani 1Akorinto15:3

__________________________________________________________

__________________________________________________________

__________________________________________________________

**10) Ukapanda kumvera Mulungu ukuyenera kuchita chiyani?**

**1 Yohane 1:9**

T_________________________machimo athu ndipo mulungu

A_________________________________________________ife machimo athu.

**11) Vesi lina limatiuza kuti tidzakhala ndi moyo wa muyaya kumwamba. Pezani mau amene akusowekera**

Werengani 1Yohane 5:13.

Izi ndakulembelani ______________________________

amene mukhulupirira dzina

la___________________________________ wa mulungu, kuti

____________________________. Mudziwe

kuti_______________________muli ndi moyo wosatha.

**12) Lembani mzele kusi kwa mau oti khristu mu mchiganizo ichi "mkhristu".**


**Lowezani ma vesi awa:**

"Koma onse omwe anamulandira iye, anawapatsa mphamvu yotchedwa ana ache kwa iwotu omwe okhulupirila dzina lache." (yohane 1:12)

"Pakuti mulungu anakonda dziko la pansi kotero kuti anapatsa mwana wake obadwa yekha kuti onse okhulupilira iye asataike koma akakhale nawo moyo osatha." (Yohane 3:16)

"Pakuti ndinapeleka kwa inu poyamba,chimeneso ndinalandila, khristu anafela zoioa zathu monga mwa malembo." (1akorinto15:3)

Musaiwale kuti munalandila yesu kukhala mbuye ndi mpulumutsi wanu. Ndikukhulupilila kuti yesu ndi mwana wa mulungu ndipo inu ndi modzi wa ana ache.



PHUZIRO 2

## KUKHALA MOYO MWA YESU

Pali njira imodzi yokha yokhalila okondwa ndiyo kukhala mwa yesu.

M'Baibulo timapezamo malamulo omwe tingatsatire kuti tikhale momwe Mulungu akufunira.


Munsimu muli malamulo ena omwe mulungu anatipatsa kuti tiwatsatire pokhala m'moyo okondwa ndi wamtendere.



Mulungu sanatifunsepo kuchita kanthu opanda kutilonjeza kuti adzatithadiza.ukaphwanya limodzi mwa malamulowa ndi bwino kumupepesa Mulungu. Nthawi zonse Mulungu amafuna kuti khululukira.

Mulungu amakukondabe ngakhale umalakwitsa.koma sikuti amasangalala ndi zoipa zomwe umachita, ngakhale kuti ndiwebe mwana wache

Umadziwa kuti anthu amaona zochimwa zako?



Ngati ulibe chitsimikizo cha zina pa moyo wako kuti zilibwino kapena ayi, udzifunse mafuso awa:

- *Kodi ndimachita ndi kuyankhula mokondweletsa Mulungu?*
- *Kodi ndi maesela kuganiza ndi ku yankhula ngati Yesu?*
- *Kodi ndimachitila ena zomwe ndimafuna ena kundichitilanso?*
- *Kodi ndimakomela mtima ndikukonda ena?*
- *Kodi ndine okonzeka kuthandiza ena?*

Zilipo nthawi zina zomwe satana adzakunyengelera kuti uchimwe.izi zikakuchitikila lankhula ndi kupempha Mulungu akuthandize.Usaiwale kuti kuyesedwa si tchimo koma kulolela maeselowo ndikuchita zoipazo.

Satana ndi m'dani wako.  Iye ndi ochenjera.  Amakonda kukunamiza kuti ulakwe. Mulungu ndiwamphamvu koposa satana.Mulungu adzakuthandiza munthawi ya nsautso.welengani 1Yohane 4:4



## Kodi mwaphunzira chiyani powelenga?

1. **Lembani malamuro asanu omwe tikuenela kukhalamo.**

   ____________________________________________________

   ____________________________________________________

   ____________________________________________________

   ____________________________________________________

2. **Kodi Mulungu adzatitani tikavomereza kulakwa kwathu** (1 Yohane1:9)

   ____________________________________________________

3. **Zungulizani mau akuti zoona kapena zabodza mziganizo zili m'musimu.**

   Anthu amaona zochita zathu. **eya/ayi**
   Anthu amamvetsera zoyankhula zathu. **eya/ayi**
   Mulungu amafuna ndikhale okoma mtima. **eya/ayi**

4. **Lembani X kumbuyo kwa chiganizo choona.**

   ______ Ndikuyenela kuyankhula ndi Mulungu tsiku ndi tsiku.
   ______ Ndikuyenela kuchita chabwino kamodzi pa sabata.
   ______ Ndikuyenela kumvera mawu a Mulungu pomwe ndafuna kutero.

5. **Ndi ndani yemwe amatipangitsa kuchita tchimo.**

   Mulungu Satana Yesu

6. **Zungulizani 'zoona' kapena 'zabodza'**

Mulungu adzandi teteza panthawi ya msautso.

**zoona/zabodza.**

Satana amandiyesa kuti ndilakwitse.

**zoona/zabodza.**

Kuesedwa ndi kuchimwa.

**zoona/zabodza.**

7. **Wamphamvu ndi wankulu kuposa satana ndi ndani?**

___ ___ ___

8. **Kodi Mulungu angatiyese?** Yakobo 1:13

_____eya _____ayi

9. **Werengani ndi kuphunzira vesi iyi**

Yohane13:35

"Mwaichi anthu adzazindikira kuti muli akuphunzira anga ngati muli ndichikondi."

10. **Kopelani vesi yapa Mateo 28:20 lomwe ndi lonjezo la mulungu kwa tonse.**

"ndili ndi inu kufikila kumapeto kwa dziko" Mateo 28:20

______________________________________


______________________________________

______________________________________

______________________________________

_________________________






## PHUNZIRO 3

# KUWERENGA BAIBULO LANU



Monga umafuna chakudya kuti ukhale ndi thanzi chomwechoso umafuna kuwerenga baibulo kuti ukule muuzimu.

Baibulo ndi uthenga wa Mulungu kwa anthu okhala pa dziko,ndi uthenga kwa misinkhu yonse,ndi buku limodzi lalikulu lomwe lili ndi mabuku 66 pamodzi_39 mchipangano cha kale ndinso 27 mchipangano cha tsopano.

Kuwelenga baibulo tsiku ndi tsiku kumakuthandiza ku:

- Dziwa za Yesu mwana wa Mulungu
- Kudziwa zomwe Mulungu amafuna kwa iwe
- Ukasikidwa ndi kukhumudwa
- Ukafuna thandizo la Mulungu popanga chiganizo
- Kukula muchikhristu.

Udziwerenga baibulo **tsiku ndi tsiku**.Ukhonzanso kuphunzira powerenga mabuku a maphunziro a kutchalichi kwanu, ndi mabuku enaso ankhani za baibulo.

Udziwelenga baibulo **palipose** pomwe uli ku nyumba, kutchalitchi, kusande sukulu, mchipinda chako chogona, kunja palipose ndi **nthawi iliyose.**

Uziwelenga baibulo **mosamala**.ngati sukumvetsetsa zomwe ukuwerengazo,mufunse mulungu kuti akuthandize kumva, ukhozanso kufunsa aphunzitsi ako kuti akuthandize kapena abusa ako pazomwe sukumvetsetsa.

Uziwerenga baibulo **monong'ona** kapena **mofuula.**ganizira zomwe Mulungu wanena kwa iwe m'mawu ake.

Udziwerenga baibulo pa **wekha kapena** ndi **ena**

**Ungayambile pati kuwerenga?**

Ukhoza kusankha kuyambira pa chiyambi ndi Genesesi,kapena chipangano cha tsopano.Koma buku la Luka m'chipangano cha tsopano ndilabwino kuliyambilira



**Kodi Waphunzira chiyani powerenga?**

1) **Tatambasulani mawu awa amene akusonyeza zomwe mukuyenera kumapanga tsopano pamene mwakhalano Mkhristu.**

_________________ ___________ _____________________

**ngareweku** **khubu** **kalitupalo**

2) **Lembani zithu ziwiri zomwe mungapindule powerenga baibulo-**

___________________________________________________________

___________________________________________________________

3) **Lembani 'X' kutsogolo kwa chiganizo cholondola .**

_____ Ndikuyenera kuwerenga baibulo tsiku ndi tsiku
_____ Ndidziwerenga baibulo ku tchalitchi kokha.
_____ Baibulo ndi mau a Mulungu.

4) **Anganditthandize ndi ndani kumvetsetsa mau a Mulungu?**

___________________________________________________________

___________________________________________________________

5) **Werenga Masalimo 119:105. Mulungu akukuuza chiyani?**

Mau anu______________________________ mapazi anga

__________________________________________njira yanga

6) **Lembani ndikuloweza ma vesi awa pa mtima.**
"Thambo ndi dziko zidzachoka koma mau anga sadzachoka ayi."

(Mateo 24:35)

______________________________________________

______________________________________________

"Ndinawabisa mawu anu mu mtima mwanga kuti ndi sachimwire inu." (Masalimo 119:11)

______________________________________________

______________________________________________


Mawu anu ndi nyali yaku mapazi anga ndikuunika kwa pa njila yanga (masalimo119:105).

______________________________________________

______________________________________________


**6) M'nyumba mwathu mungapezemo_________mabaibulo**

**7) Lembani kalata kwa mulungu mumuuze chomwe baibulo limatanthauza kwa inu**




**8) Vesi langa la pamtima ndi**

______________________________________________



**PHUNZIRO 4**

## KUYANKHULA NDI MULUNGU

Kuyankhula ndi Mulungu atate wako wakumwamba kumatchedwa 'pemphero'. Ndikofunikila kwambiri kuti uziyankhula naye pafupi pafupi, monga momwe akunenela pa 1Akolose 5:17. Kuti "penphelani kosalekeza". Tikuenela kupemphera nthawi iliyose, pena palipose.

Mulungu amamva pempho lathu nthawi iliyose kaya ukunong'ona kapena ukufuula. Mulungu sagona komanso saodzera, ukhoza kumuyankhula usiku kapena masana iye satanganidwa.

*Nthawi zina zomwe ungapemphere ndi izi:*

- Ukamayamba tsiku lina-----upemphe Mulungu akutsogolere.
- Usanayambe kudya-----muthokoze pa chakudya.
- Ukachita mantha-----mupemphe akulimbikitse.
- Ukasikidwa-----muuze akusangalatse.
- Ukasowa----mupemphe ndi kukhulupilira kuti akwaniritsa chosowacho.
- Ukachimwa----- upemphe  akukhululukile

- Ukadwala----- upemphe machiritso.
- Ukafuna thandizo---- umupemphe akuthandize.
- Usanagone----- umupemphe chitetezo.

*Izi ndi zina zomwe ungatsatile pomphera.*

- Muthokoze pa zapadera zomwe wakuchitira
- Kumbukira banja lako, mpingo wako, anzako, abusa ako,ndi amishoni anu.
- Muuze Mulungu za zovuta ndi zofuna zako.
- Pomaliza pa pemphero lako nena mawu awa "mu dzina la Yesu". (Yohane 14:13, 14).

Yesu anaphunzitsa ophuzira ake momwe anga pemphelere; pa Mateyo 6:9-13, iye anapereka chitsanzo cha pemphero.



*"Atate athu akumwamba dzina lanu liyeretsedwe, ufumu wanu udze. Kufuna kwanu kuchitidwe, monga kumwamba, chomwecho pansi pano. Mutipatse ife lero chakudya chathu. Mutikhulululukire zochimwa zathu. Musatitengere kokatiyesa koma mutipulumutse kwa oipayo. Pakuti wanu uli ufumu ndi mphamvu ndi ulemelero wanthawi zones. Ameni"*

Nthawi zina ukhoza kumapemphera ndi anzako koma ndi bwino kuti udzikhala ndi nthawi yako yapadera ndi Mulungu. Mkofunikila kumayankhula ndi Mulungu monga umayankhula ndi anzako.

Ukhoza kupemphera pawekha m'chipindachako, m'galimoto, kusukulu, kutchalitchi, palipose nthawi iliyose, malo aliwose. Nthawi zina utha kupemphera utagwadwa, nthawi zina ukhoza ku tseka maso, pagulu mutha kugwilana manja, mutaimilira ndi kugwilana manja mozungulira.

Musaiwale kuti Mulungu amayankha mapemphero anthu njira zitatu: monga **EYA** nthawi zina **AYI** komaso nthawi zina **DIKILA**. NTHAWI ZOSE Mulungu amasunga malonjezano ake khalani ndichitsimikizo paizi.pa Aroma 4:21, timawerenga mawu awa: 'nakhazikitsaso muntima kuti chimene iye analonjeza analinayonso mphamvu yakuchichita'.




Baibulo limatiuza kuti tizipempherela anzathu komaso tizipemphelera otizunza.

Yakobo 5:16 "Pemphereranani wina ndinzache ndipo pemphero la olungama limachita koposa."

Mateu 5:44 "Kondani adani anu ndi onse okuzunzani."

## Kodi mwaphunzira chiyani powerenga?

1. **Kuyankhula ndi mulungu ndi chaini? Lembani X kutsogolo kwa yankho lolondola.**

    ____ kuimba

    ____ kupemphera

    ____ kuwerenga

2. **Kodi 1 Petulo 3:12 amakamba zotani za pemphero lathu?**

    Maso ake

    ________________________________________________

    Makutu ake

    ________________________________________________

3. **Ndi nthawi yanji yomwe unga yankhule ndi Mulungu?**______________________

4. **Ungayankhule naye kuti Mulungu?**_____________________________________

5. **Chongani pa chiganizo choona**

______ Ndingayankhule ndi Mulungu nthawi iliyose, palipose.

______ Nthawi zina Mulungu amatanganiwa kuti sangamve pemphero lathu.

_____ Sindikuyenera kupemphera ndi ena.

_____ Kulapa ndikuvomeleza zolakwa zathu ndi Mulungu.

______ Ndikuyenera ku mawapemphelera amzanga.

______ Kupemphera tsiku ndi tsiku ndilo khalidwe labwino.

6. **Werenga mokweza ndikuloweza pemphero la ambuye pa Mateyo 6:9.**

7. **Zungulizani yankho lolondola m'musimu.**

Nthawi zonse ndikuyenera kugwada popemphera

**zoona/zabodza**

Pemphero ndiku yankhula ndi Mulungu.

**Zoona/zabodza.**

Ndikhoza kuyankhula ndi Mulungu nthawi iliyose kulikose.

**zoona/zabodza.**



**PHUNZIRO 5**

## Malo opembedzela

Amodzi mwa malo omwe tingaphunzilire za Yesu ndi Mulungu ndi ku tchalitchi.

Tchalitchi imatchedwaso nyumba ya Mulungu ndimalo omwe anthu amisinkhu yonse amasonkhanako kudza;

1. Pembedza ndi ku lemekeza Mulungu.
2. Phunzila zochuluka zokhudza Mulungu ndi mwana wake Yesu.
3. Kumana ndi akhristu anzawo.
4. Khala pamodzi ndi banja lawo la Mulungu.
5. Imba, pemphera ndi kudzaphunzira.
6. Kudza chitila umboni pa zomwe Mulungu watichitila.
7. Chiyanjano cha akhristu.
8. Kuphunzira ku sande sukuklu.
9. Kuphunzitsidwa baibulo.

Kupezeka nawo pa mpingo sabata ndi sabata ndi kuchita nawo zapa mpingopo kungakupangeni kuphunzira zambili za baibulo, lomwe ndi mawu a Mulungu.

Alipo aphunzitsi ena omwe adzakuphuzitseni m'misonkhano ya chinyamata, ndi m'misonkhano ina yosiyana.kuphuzila za Mulungu kungakupangeni kukhala olimba mchikhristu ndi kukula .choncho ndi chifukwa chake uyenela ku pezeka ku mpingo sabata ndi sabata.

Ngakhale kuti lasabata ndilomwe ambiri amapita kukapembedza.komaso pali masiku ena mkati mwasabata omwe ukuyeneranso kumapezeka ku tchalitchi ngati kuli zochitika zina.


Mawu a Mulungu amatilimbikitsa kusonkhana pa modzi ndi anzathu ku tchalitchi. Ahebri 10:25.

*Ndi chifukwa chiani tiyenera kupita ku tchalitchi?* Ili ndi funso lomwe achinyamata ambiri amafunsa, ena mwa mayankho ndi awa:

1. Baibulo limatiuza kuti tizisonkhana pa modzi ndi anzathu
2. Timakula ndi kumudziwa ambuye ngati tikuva ziphuzitso ndi mauthenga amulungu.
3. Timakumana ndi kudziwana ndi akhristu anzathu.
4. Timayenera kukhala ndi chiyanjano ndi akhristu anzathu.
5. Timayenera kukhala ndi nthawi yopereka malingaliro athu kwa mulungu.
6. Timayenera kugawana chikondi chathu cha pa mulungu.

Zilipo zambiri zomwe tingachite ku tchalitchi. Mukasonkhana ndi ena mukhoza kumu lemekeza limodzi pamalo amodzi. Izi ndi zinthu zisanu ndi zitatu zomwe munga chite ku tchalitchi kwanu.

Ukamapita ku tchalitchi tengani baibulo ndi ndalama ya chopereka




Chifukwa chakuti ndinu chiwalo cha mpingo wanu mukuyenera kuthandizira ntchito zina ngati kusesa.

Udziwauzanso ena ndiku waitanila ena ku tchalitchi kwanu.

Kuphunzira za Mulungu ndi kwabwino ndikosangalatsa. Kupita ku tchalitchi chikhale chizolowezi chanu. Zidzakuthandizani kukhala moyo womwe yesu akufuna kuti mukhale.

## Kodi waphunzirapo chiyani powerenga?

1. **Mpingo ndi chiyani** (lembani **X** pa chiganizo choona)
   _____malo openphelela.

   _____malo oimbila ndi kulambira.

   _____malo ophuzilira za mulungu.

   _____malo ochitira ndewu.

2. **Malizitsani vesi iyi (Aheberi 10:25).**
   "osaleka____________________________________________

3. **Chongani eya kapena ayi**

| | |
|---|---|
| Kodi ndizipita ku tchalitchi kulikose? | **Eya/ayi** |
| Kodi ndizipita ku tchalitchi sabata ndi sabata? | **Eya/ayi** |
| Kodi ndingaitanile ena ku tchalitchi? | **Eya/ayi** |

4. **Kodi malo abwino kukumana ndi abwezi ndi kuti?**

   ____________________________________________

5. **Lembani zithu zisanu ndi zitatu zomwe zimachitika ku tchalitchi.**

   ____________________________________________

   ____________________________________________

   ____________________________________________

   ____________________________________________

6. **Nenani zithu ziwiri zomwe mukuenela kutenga ku tchalitchi**

   ____________________________________________

7. **Kodi umava bwanji ukamatuluka mu tchalitchi**

   ____________________________________________

8. **Kodi dzina la tchalitchi yako ndi chiyani?**

____________________________________________

9. **Dzina la abusa anu ndi ndani**

____________________________________________

10. **Ndiziti zina zomwe zimachitika ku tchalitchi kwanu?**

______________________________

______________________________

______________________________

______________________________

______________________________

______________________________



**Ndikhoza kuthandiza mpingo wanga pochita zinthu ngati izi:**



Kuse________________.

kuuza ena za_______________.

kuitanila ena ku_________________.



**Lowezani vesi ili**:

"chikhulupiliro chimabwela ndi kuva  mawu a Mulungu" Aroma 10:17



"Yambani mwa thanga ufumu wake ndi chilungamo chake ndipo zones zidzaonjezelewa kwa inu."

- Mateyo 6:33



**PHUZIRO 6**

## KUUZA ENA ZA YESU

Tsopano pokhala mwana wa Mulungu ukuenelaso kuuza ena za Yesu. Ukuenela kukhala mmodzi wa iwo omwe amachitila umboni ena pa zomwe mulungu wawachitila.

Pa Mariko 5:19, Yesu akuti 'pita kwa abale ako ukawauze zomwe mulungu wakuchitilazi ndi chifundo chake pa iwe'. Tonse tili nawo anzathu ndi abale.

Omwe samudziwa Mulungu, yesetsani kugawana nawo za Mulungu. Ndizomwe wakuchitilani.

Pano pali zomwe muenela kudziwa usana yambe kuchitila ena umboni za Yesu.

1. Dziwa kuti ndiwe khristu (Yohane 5:24)
2. Dziwa kuti mulungu amakonda aliyese. (Yohane 3:16)
3. Dziwa kuti aliyese anachimwapo. (Aroma 3:23)
4. Dziwa kuti aliyese amaenela kuvomeleza machimo ake kwa Yesu. (1Yohane 1:19)
5. Dziwa kuti mulungu analonjeza moyo osatha kwa okhulupilira onse. (Aroma 6:23)

6. Dziwa kuti yesu ndiokozeka kulandila aliyese opemphayo. (Mateyu 21:22)


M'modzi mwa abale ako kapena anzako akavomeleza machimo awo ndikuwasiye. Yesu adzmukhulululukira ndipo adza khalaso m'modzi wa am'banja la Mulungu monga ulili iwe. Usaiwale kuti yesu anafela aliyese pa dziko.

*Gawana nawo anzako achi khristu kufunika kwa-*

1. Kuwelenga baibulo tsiku ndi tsiku
2. Kuyankhula ndi mulungu tsiku ndi tsiku
3. Kupita kusande sukulu ndi ku tchalitchi pafupi pafupi
4. Kuuza ena  za Yesu
5. Kuonetsela moyo wa chikhritsu kwa ena.

*Pali njila zambiri zomwe ungagwilitse ntchito pouza ena za Yesu. Monga:*

1) Kugwilitsa nthito mau ako powa uza zomwe Mulungu wakuchitila.
2) Popeleka ma pepala okhala ndi uthenga (ma tracts).



3) Kukhala moyo wa chikhristu.
4) Kuwaitanila ku tchalitchi kwanu.
5) Kuwalembela kalata kapena chidziwitso pa za Yesu.

Yesu amafuna tikhale kumuchitila umboni, kodi ife angatidalile?

Inde Yesu angadalile ______________________________
kukhala mboni yake. (lemba dzina lako)

## Kodi mwaphuzila chiani powelenga?

1. **Ndipati pomwe timapeza vesi lonena kuti tipite tikauuze ena za Yesu m'baubulo.**

    ___________________________________________________________

2. **Lembani 'eya' kapena 'ayi' kumapeto kwa ziganizo izi:**

    Aliyese anachimwa?________

    Mulungu amakonda aliyense?_______

    Aliyense akuyenela kulapa?_________

    Nthawi zose yesu adzatikhulukila._______

3. **Kodi ungamuuze chiyani mkristu watsopano? Chongani yankho lolondola.**
    - Kupemphera lasabata lokha._____
    - Kuwerenga baibulo tsiku ndi tsiku.____
    - Kupita ku tchalitchi lasabata lokha._____
    - Kuuza ena za yesu.____
    - Kuonetsa moyo wachikristu kwa ena._____

4. **Lembani njira ziwiri zomwe tingauzire ena za Yesu____________________________________**

5. **Ena tiwauze za yesu chifukwa chiyani?________________________________**

6. **Lemba maina a anthu atatu omwe ukawauze za Yesu.**

    ______________________

    ______________________

    ______________________

7. **Lemba zithu zitatu zomwe ukuyenera kudziwa usanachitire ena umboni.**

8. **Lemba mavesi pamodzi ndi buku, chaputala zomwe zingakuthandize kuchitira ena umboni.**





9. **Kumbukira mavesi omwe wasunga pamtima**

10. **Loweza vesi iyi Yohane14:6**

Mavesi ofunika kwambiri mubuku loseli ndi awa, amene mungafune kuwasunga pamtima:

Luka 2:52

Mateyu 24:35

Yohane 3:36

1 Yohane1:9

Mariko 11:24

Mateyu 6:9

Ngati wamaliza bukuli pititsa kwa aphuzitsi ako akaone zomwe wayankha ndipo akayankha adzakubwezeranso.

